ttb_**Nya_0832_script**

1 Atesalonika : 4:13-18

Mutu : Ziphunzitso zina zokhudzaMkwaturo

Ndipereka moni kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero titsogozedwe ndi mau apa 1 Petro 2:21, amene akuti, "PakutinsoKristu anamva zowawa m'malo mwanu, nakusiyirani chitsanzo kuti mukalondole mapazi ake."

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula1 Atesalonika 4:13, m'mene timakambirana za chitonthozo cha chiyembekezo pakubweransokwa Yesu Kristu. Ndipo lero pa 1 Atesalonika 4:13-18, tikambirana za ziphunzitso zina zokhudzamkwaturo.

13. Koma sitifuna, abale kuti mukhale osadziwa za iwoakugona; kuti mungalire monganso otsalawo, amene alibe chiyembekezo.

Atesalonika adaliokhudzidwandi chomwe chidzachitika kwa oyera mtima amene adafamkwaturousadachitike. Ganizo ili, linalipo chifukwa Paulo amaphunzitsamwachimvekere kuti kubweranso kwa Ambuye kudzatenga okhulupirirakwayandikira. Tsono ngati okhulupirira ena adamwalira nkhawa inali yakuti mwina amene adamwalirawoasemphana ndi mkwatulo.

Wokondedwa anzanga apauleondo, nkhani ikunena kuti kubwera kwa Yesu kwayandikira ndithu, ndipo monga adaphunzitsa Paulo leronsondichimodzimodzi. Koma ngoziili pakuti anthu ena amafuna kulosera kuti tsiku lake ndi lakuti. Palibe amene amadziwa za tsikulo.Palibe amene adziwaza tsiku kapena nthawi yake.Kulosera za tsikulo kapena nthawi ndikusonezeka chabe.Koma Paulo akuyankha nkhawa imene Atesalonika anali nayo yokhudza abale amene adaliatamwalira.

14. Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi Iye,iwoakugona mwa Yesu.

Paulo akunena kuti "Yesu adafanaukanso."Sakunena kuti Yesu adagona, akunena kuti Yesu adafa ndipo wokhulupirira 'amagona'.Pano tiyenera kumvetsetsa chimene akunena apa;

Mu Buku Lopatulika timapeza mitundu itatu ya imfa.Imfa yoyamba ndi kufa kwa thupi kumene kuli kulekana kwa thupi ndi mzimu wa munthu. Kachiwiri Paulo akufotokoza kuti kukhala munthu woyenda monga mwachifuniro cha thupi,ndiye munthu amene ndi

wakufa ku uzimu.Ndiye pali imfa ya uzimu imene ndikulekana kwa munthu ndi Mulungu. Imfa iyi ndi imene idachitika m'munda waEdeni pamene Mulungu adanena kuti munthu adzafa ndithu akadzadya chipatso chapakati pa munda uja. Munthu adalekana ndi Mulungu.Adamu adabisala, ndipo adathawaatamva Mulungu akuyendam'mundamo.Uku kunali kulekana pakati pa Mulungu ndi munthu.Adamu ndi Havaadafa tsiku limene adadya chipatso; adafa imfa yauzimu.

Paulo adalankhulapo za imfa ya uzimu pa Aefeso 2:1 pamene adati: "Ndipo inu adakupatsani moyo, pokhala mudali akufa ndi zolakwa ndi zochimwazanu."Pali anthu zikwizikwi amene akuyenda lero lino,koma ndi akufa chifukwa akukhala m'moyo wolekana ndi Mulungu.Tsono imfa yachitatuyi ndi imfa yomwe imabweretsa imfa ya nthawiyamuyaya.Iyi ndi imfa yomwe timawerenga pa Chibvumbulutso 20:14, pamene pali mau akuti, "Ndipo imfa ndi Hade zidaponyedwam'nyanja yamoto. Iyi ndiyo imfa yachiwiri, ndiyo nyanja yamoto."

15. Pakuti ichi tinenakwa inu m'mawu wa Ambuye, kuti ife wokhala ndi moyo, otsalira kufikira kufikanso kwa Ambuye, sitidzatsogolerawogonawo.

Poyamba pano Paulo akugwira mau akuti, "Pakuti ichi tinena kwa inu m'mawua Ambuye." Kutsindika kuti sakufuna kunena maganizo ake pa nkhaniyi. Pachifukwa chimenechi akutsimikiza kuti chimene akunena iye kwa Atesalonika ndi mau ya Ambuye. Paulo akudziwankhawa ya Atesalonika kuti akufunitsitsakuti amvetsetse chimene chidzachitikekwa anthu amene adafamkwatulousanachitike. Tsono poyankha monga mwa mau aAmbuye,Paulo akuwawonetsa kuti akufa mwa Ambuye adzaukitsidwa pa tsiku la mkwatulo. Amene adafa mwa Ambuye sadzasiyidwa pa mkwatulo.

Kachiwiri Paulo akunena kuti, "Ife wokhala ndi moyo, otsalira kufikira kufikansokwa Ambuye, sitidzatsogolerawogonawo." Amene adzakhale ndi moyo patsikulosadzatsogolera amene adagona ayi, koma iwo amene adafa ndiwo amene adzaukitsidwendikutengedwamotsogolera amene adzakhale ndi moyo panthawiyo.

16. Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mfuwu, ndi mawuam'ngelowamkulu, ndi lipenga la Mulungu: ndipo akufa mwa Khristuadzawukachoyamba.

Pano Paulo akupereka mau achilimbikitso pamene akuti, "Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha."Nkhani ikunena kutiYesuadzabwera yekha sadzatuma angelo. Mawu a Yesu Khristuadzamveka ngati a m'ngelowamkulu kapena ngati lipenga. Yesu adzatumaangelo ku mphepo zonse zinayi za dziko lapansi,kudzasonkhanitsaosankhidwa ake, amene adzakhale anthu amitundu yonse. Koma pamene adzabwera panthawi ya mkwatulosadzatumaangelo ayi.

Angelo ndiwo amene anatumikirapakulengeza za kubadwa kwa Yesu. Koma funso nkumati: kodi adalengeza zotani za Yesu nthawi yakubadwa kwake?Angelo adalengeza kuti kwabadwa Mwana wa Davide, Mfumu yolonjezedwa. Adalengeza za kubadwa kwa Mfumu. Anzeru aku m'mawa amafufuza kumene Mfumu ya Ayuda, inabadwira. Kutsimikiza kuti angelo ndiwo amene anatumikira kuti Israeli adziwe za kudza kwa Mpulumutsi osati kuuzampingo pa tsiku la mkwaturo ayi. Taonani kuti pokhazikitsa mpingo pa tsiku la Pentekoste panalibe angelo. Mzimu Woyera

Mwini wake ndiye ameneadatsika. Podzatenga mpingo wake kuchoka padziko lapansi Ambuye Mwiniwake adzatsika kuchokera Kumwamba.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti patsiku la mkwaturo, Ambuye mwini atsatsika yekha osatumaangelo ayi. Iye, adzatsika monga momwe adamuonaophunzira ake akukweraKumwamba, koma patsiku limeneli adzatsika ndi ulemelero.Kodi inu muli kukonzekera motani za tsiku limeneli?

Tsono mwina inu mkufunsa kuti,nangam'ngelo uyu akupezeka bwanji popeza poyambamwanena kuti sipadzakhalam'ngelo pa mkwatulo?Anzanga, ndifuna mumvetsetsenkhani ikuti mau a Ambuye adzamveka ngati mau a m'ngelowamkulu. Kutanthauza kuti simawuam'ngelo amene adzamvekowo ayi, koma mawuwoadzamveka ngati a m'ngelowamkulu. Yesu Mwini wake adzatsika ndi mau akulu ngati momwe amakuwira wolamulira asirikali ankhondo.Ndipo ndilipenga la Mulungu, limene lidzawombedwa pa tsiku lobwerakwa Ambuye.

Ayudaamayimbalipengaakafunakusonkhana monga masiku ano mipingoinaimayimbabelu (Levitiko 25:9; Numeri 10:2). Choncho pakati pa Ayuda akamva kuyimba kwalipengazimatanthauza kuti ayenerakusonkhana. Tsono nkhani ikunena kuti Mulungu amatilankhula kudzera mwa zinthu zimene tikhoza kuzimvetsetsamosabvuta.Ndiye chimene chimachitika ndi chakuti a Yuda, pa nthawi ya mtendere amayimbalipengalosakweza kwambiri.Koma panthawi ya nkhondo lipengalimaliramokweza kwambiri.Ndiye pa Tsiku lakubweransokwa Ambuye lidzakhala tsiku lachigonjetso. Kotero kuti ndichifukwa chake pa tsikuli padzakhala mfuwu, waukulu wongawalipenga. Kutsindika kunena kuti, pa tsikulisipadzakhalalipenga, koma mfuwuwa ulamuliro udzamveka ngati lipenga. Kodi tikudziwa bwanji kuti sipadzakhalalipenga? Yohane aliyekhayekha pa chisumbu cha Patimo adalemba kuti: “Ndidagwidwa ndi Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndipo ndidamva kumbuyo kwanga mawuakulu, ngati a lipenga” (Chibvumbulutso 1:10). Ndipo pamene Yohane adatembenuka kuti awone kuti adamva mau andani,iyeadawona Yesu mu ulemelero wake.Kutsimikiza kuti chimene chidamveka ndi mau akulu ngati lipenga anali mau a Ambuye mu ulemelero wake.

Tsono anthu ena amaganiza kuti amene adzayimbelipenga ndi m'ngelo Gabrieli kapena Mikayeli. Nkhani ikuti ngakhale angelo atakhala kuti ali ndi malipenga koma pa tsiku limeneli Ambuye sadzafuna thandizo la angelo kuyimba lipengakuyitana anthu ake. Yesu mwini wake adzalamula anthu ake ndi mau akulu amene adzamveka ndi mfuwu waukulu ngati lipenga.Nkhani ikuti zidzakhala ngati muja Ambuye Yesu ananena ndi mau aulamuliropa manda a Lazaro.Lazaro anaturukam'manda ndi mau aulamuliro osati ndi chithandizo cham'ngeloayi. Ambuye mwini wake adzatsika yekha ndi mau akulu amene adzamveke ngati lipenga ndipo akufa mwa Ambuye adzauka.Kutanthauza kuti Mkwaturoudzachitika mwa dongosolo.Tikunena kuti anthu onse akufa mwa Khristuadzawukapoyamba.Wokhulupirira adzauka koyambirirakutanthauza kuti akufa mwa Ambuye adzauka ndipo kutsatira pamenepo amene adzakhale ndi moyo adzatengedwa.Kutsimikiza kuti inu ndi ine, ngati wokhulupirira tidzakhudzidwa ndi mkwaturowo.

17. Pamenepo ife wokhala ndi moyo wotsalafetidzakwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye

mumlengalenga, ndipo poterotidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.

Tsono pamene tinena za “kukwatulidwa” tikutanthauza za kutengedwa m’mwamba ndi mphamvu kapena mwa kutsompholedwa.Koma patsiku la mkwatulo zinthu zidzachitika mwadongosolo.Akufa mwa Ambuye adzauka moyambilira.Tere, chikhulupiriro ndi chakuti Sitifano uja adaponyedwamiyala adzauka.Mwina adzakhala patsogolo pa atumwi chifukwa ndiye adayamba kufa.Atumwi ndi okhulupirira onse amene adafa, ena chifukwa chachikhulupiriro chawo onse adzauka.Pomaliza amene adzakhale ndi moyo panthawiyoadzatsatira pambuyo pa amene adafa mwa Ambuye.Amoyo adzakhala pambuyo pa onse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikutsindika kunena kuti tonse tidzakwatulidwa. Kutanthauza kuti tidzatengedwa mwa mphamvu ya Mulungu osati mphamvu yaife tokha ayi. Iyi, ndi mphamvu ija inatengaFilipopa Machitidwe 8:39, pamene akuti, “Ndipo pamene anakwerakuturukam’madzi, Mzimu wa Ambuye anakwatulaFilipo; ndipo mdindosanamuonanso, pakuti anapita njira yake wokondwera.”Kunena kuti Filipoadatengedwa kapena kukwaturidwa ndi Mzimu Woyera.Filiposanagwiritse ntchito

mphamvu yake kuti achoke pamene anali kupita malo ena, koma adanyamulidwa ndi mphamvu ya Mzimu wa Ambuye. Chomwechonso pa tsiku limeneli matupi athu adzanyamulidwa ndi mphamvu ya Ambuye kukakumana naye mu mlengalenga. Mphamvu yomweyiidzaukitsa akufa mwa Ambuye komanso kunyamula onse pamodzi ndi okhulupiriraamene adzakhaleali ndi moyo kunka kukakumana ndi Ambuye mu mlengalenga.

Tsono pamene tinena za kukakumana ndi Ambuye mumlengalenga, tikunena kuti tidzakumana ndi Ambuye m'Mwambam'mitambo.Tamveraniokondedwa kuti pakubwera Yesu kachiwiri, inu ndi ine, tidzakumana naye mumlengalenga osati pansi pano ayi.Ichi, ndi chithunzi chochititsa chidwi kwambiri, kotero kuti pobweranso Ambuye sadzachitakufikanso pansi pa nthaka ayi, koma adzayima mu mlengalenga kumeneadzakumane ndi okhulupirira.Ndiye tikunenetsa kuti pamene tiwerengamau a Mulungu, palibe pamene timamva kuti chiweruzo chidzachitika pansi pano. Pachifukwa ichi mwini wake akadzafikaadzakumana ndi anthu ake mu mlengalenga.Kumene tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse sakutanthauza kuti tidzakhala ndi Ambuye mu

mlengalenga. Kumbukirani kuti okhulupirira adzakhala ndi Ambuye Kumwamba kumene Ambuye adapitakukakonza malo. Ndipo pa Mateyu 25:34 timawerenga kuti; “Pomwepo Mfumuyoidzanenakwa iwo a kudzanja lake lamanja, Idzani kuno inu wodalitsika wa Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi.”Kutanthauza kuti atanthamayesero ndi mazunzo adziko lino lapansi, oyera mtima onseadzalowaKumwamba ku ulemelerowa Mulungu Atate kumene Ambuye Yesu akutikonzera malo tsopano. Potero tidzakhala ndi Ambuye mu Ufumu wa Mulungu Atate.

18. Chomwecho, tonthozanani wina ndi mzake ndi mawu awa.

Pano tiyambe ndi mau akuti chiphunzitso cha kubweranso kwa Ambuye Yesu sinkhaniyowopsezera anthu koma yotonthozerana wina ndi mzake. Ndiye mau akuti ‘tonthozanani’ pa vesi 18 akugwiritsidwa ntchito motilangiza ndikutilimbikitsa kuti tizikambiranaa wina ndi mzake za tsiku limenelo.

Tere, mau onse opezeka pa 1 Atesalonika 4:13-18, ndi mau achitonthozokwa anthu okhulupirira, komanso opatsa chiyembekezo pa za iwo amene adagona mwa Ambuye. Kunena

kuti inu ndi ine, tiyenera kukhala ndi chiyembekezo chakuti abale athu amene adagona mwa Ambuye sadzakhalam'manda mpaka muyaya ayi.Adzawuka patsiku lobwera Ambuye ndipo adzakwatulidwa pamodzi ndi amene adzakhale ndi moyo tsikulokukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. Ndipo kuchokera tsikulookhulupirira onse akufa ndi amoyo tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse!

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani yonseyi ikutsindika kunena kuti onse oyera mtima adzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Adzakhala ndi Ambuye ku ulemelero wake Kumwamba mongaadalonjeza Ambuye pa Yohane 14:3 pamene adati: "Ndipo ngati ndipitakukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso."Kukhala ndi Ambuye ndi madalitso akuluzedi.Kumenekokulibe uchimo, kulibe masautso, kulibe choopsa chirichonse ngakhalenso imfa. Kukhala ndi Ambuye ndi malo a mpumulo weniweni, kotero kuti Kumwamba ndi malo amene tikapumuladi ku zolemetsa za dziko lapansi.Kodi inu mwatopanalo dziko lapansi? Muyenera kukhala ndi chikhulupiriro

ndi chiyembekezo cha kumbweransokwa Ambuye kudzakutengani kunka nanu kwawo.

Tsono tikunenetsa kuti kukhala ndi Ambuye, ndinkhaniyotonthoza chifukwa kumenekotikakumana ndi anzathu amene adagona mwa Ambuye. Tsiku lachitonthozo likudza pamene tidzawonana maso ndi maso ndi Mpulumutsi wathu amene adatikondaifenapereka moyo wake chifukwa cha ife. Tsiku limeneli ndi tsiku lachiyembekezo limene tidzabvala zobvala zoyera ndipo tidzasonkhana pamodzi ndi onse amene anakhulupirira Ambuye zaka zikwizikwizadapitazo ndi zomwe zilinkudza.

Tsono mwina muli kakasi ndipo muli kufunsa kuti, kodi ndani angatonthozedwe?Yankho likuti,aliyense amene Mzimu wa Mulungu ukumuchitira umboni kuti ndiwoyeretsedwa ndi mwazi wa Ambuye Yesu Kristu. Tere, mau awa ndiwopatsachitonthozokwa onse amene ali ndi njala ndi ludzulachilungamo. Mau awa ndiwopatsachitonthozokwa iwo amene akufunafuna ufumu wa Mulungu ndi chiyero chake. Ngati muli m'modzi wa anthu otere khalani nako kulimbika mtima

chifukwa patsikulo Ambuye sadzatenga aliyense amene machimo ake ndiwosakhulukidwawosasambitsidwakuchoyipa chake ayi. Kudzakhalakosatheka pa tsikulo kuti mutengedwem'machimoanu.Ndiye tikunena kuti inu ndiyo nthawi yofunafuna chipulumutso, osati pa tsikulo ayi. Tsono ngati simunampeze Ambuye muyitaneni lero pakuti aliyense amene ayitanira pa dzina lake adzapulumuka.

Pamene tikutsiriza tiyeni titonthozane wina ndi mzakemwakuphunzitsana wina ndi mzakepokambirana za tsiku limeneli.Ndiye tikutsindika kuti Ambuye Yesu akubwera kudzatenga anthu ake tsiku lina.Onse akufa mwa Ambuye adzauka ndipo amene adzakhale ndi moyo tsiku limenelo, onse adzakwatulidwa pamodzi kunka kukamana ndi Ambuye mu mlengalenga.Patsikulotidzalowamuulemelerowa Ambuye ndipo tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Pachifukwa chimenechi, tiyenera kukangalika pa kutonthozana wina ndi mnzakendikuphunzitsanamwachiyembezokuti anthu onse amene anafa ali ndi chikhulupiriro mwa Ambuye, sadzakhalam'manda nthawi zonse.Komanso pamene adzauka sadzakhala pansi pa

wokhulupirira ena ayi.Kutsimikiza kuti wokhulupirira onse adzakhala wofanana nthawi imeneyo.Koma chimene chingawasiyanitse ndi mphoto yomwe wokhulupirira aliyense adzalandira malinga ndi ntchito yomwe anagwira pansi pano.Potero tidzakhala ndi chiyembekezo chopatsachitonthozo. Chiyembekezo cha ulemelero popeza tidzakhala ndi Ambuye Yesu kwa nthawi yamuyaya. Tsono kukhala ndi Ambuye Yesu Kristu ndi chinthu cholimbikitsa kwambiri, chifukwa ndicho chitsimikizo chakuti inu ndi ine, sitidzachimwanso, sitidzabvutikanso kapena kuopsezedwa ndi chinthu chilichonse ngakhale imfa imene. Ichi, ndicho chikhalechitonthozokwa wina aliyense wokhulupirira.

Lero tilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 1 Atesalonika 4:13-18, momwe timakambirana za ziphunzitso zina zokhudzamkwaturo. Ambuye akudalitseni inu pamene muyembekezera tsiku ilo, lomwe Ambuye adzakutengani kunka kwawo. Amen!